NYA_TTB_0944_20161110_**script**

Danieli : 12:1-13

Mutu : Chibvuto cha chikulu ndi kutseka ulosi

Landirani moni wa Kumwamba, inu wokondedwa anzanga apaulendo. Lero tiyamba ndi mau a Mulungu opezeka pa Luka 18:7-8, amene akuti, “Ndipo kodi Mulungu sadzachitira chilungamo osankhidwa ake akumuitana usana ndi usiku, popeza aleza nawo mtima? Ndinena ndi inu, adzawachitira chilungamo posachedwa.Koma Mwana wa munthu pakudza Iye, adzapeza chikhulupiriro pa dziko lapansi kodi?”

Mupologalamu yatha tinali kusanthula Danieli 11:37-45, momwe timaona za ufumu wodziika kuti ndiwo wanthawiyapang’ono. Ndipo lero pamene tikutsiriza bukuli, tisanthula Danieli 12:1-13, momwe tikambirana za Chibvuto chachikulu ndi kutseka ulosi.

Danieli 12

Chapter 12, ndi chomwe chikutsiriza masomphenya amene anayamba m’chapter 10.Awa, ndi masomphenya amodzi omwe pano akumangiririkakotsiriza.Mwachisoni kuti anthu ena amatanthauziramasomphenyawa monga momwe afuna. Koma

tiyenera kudziwa kuti awa, ndi masomphenya amodzi, amene tinauzidwa pa Danieli 10:14, mau akuti, “Ndadzera tsono kukuzindikiritsachodzagwera anthu a mtundu wako masiku otsiriza; pakuti masomphenyawo ndiwo a masiku a m’tsogolo.” Tsono kuchokera ku mau amenewa ndifuna tione zinthu zitatu zomwe ndizofunika m’ndime imeneyi:

Poyamba pamene tiona mau akuti, “anthu amtundu wako,” tiyenera kuzindikira kuti ndichinthu chomwe chikukhudza kapena kudzachitikira mtundu wa Israeli pamene mpingo udzakhalautakwaturidwa kale kuchoka pansi pano.

Kachiwiri; tikagwira mau akuti, “Masiku otsiriza,” ndiwo masiku amene akugwirizana ndi masiku otsiriza a m’Chipangano Chatsopano, amene Ambuye wathu Yesu Kristu akuwatchula kuti ndiwo masiku chibvuto chachikulu (Great Tribulation), amene adzagwirizana sabata la khumi, chisanu ndi chiwiri la Danieli.

Kachitatu; tigwire mau akuti, “Pakuti masomphenya ndiwo a masiku a m’tsogolo.” Kutanthauza kuti padzakhala masiku ambiri kufika pamasikua m’tsogolo. Tikunena kuti papita kale zaka zoposera 2,500 kuyambira pomwe Danieli adaona masomphenya

amenewa. Ndiye sindikudziwa ngati tiri kuyenda m'masiku amenewa, koma tiyenera kudziwa kuti chisautso chisanayambe, mpingo wa Mulungu udzakhalautachotsedwa kale, chimene ndicho chinthu chotsatiram'chikonzero cha Mulungu. Koma tikunenetsa kuti pakali pano tiribe tsiku lomwe zidzachitikira zimenezi ndipo ngati munthu wina angakupatseni tsiku leni-leni, ndiye kuti akunena zina zosakhala m'mau a Mulungu.

1. Ndipo nthawi yomweyo adzauka Mikaelikalonga wamkuru wakutumikira ana a anthu a mtundu wako; ndipo padzakhala nthawi ya masautso, siinakhalayotere kuyambira mtundu wa anthu kufikira nthawi yomwe ija; ndipo nthawi yomweyo anthu ako adzapulumutsidwa, yense amene ampeza wolembedwa m'buku.

Pano tiyeni tiyambe ndi mau funso lakuti, pamene tinena kuti ndiwo masiku otsiriza, tikunena zimenezi ndi ulamuliro wa ndani? Yankho likuti, tikunena ndi ulamuliro wa Ambuye wathu Yesu Kristu, amene anagwiritsanso mau omwe Danieli akugwiritsa ntchito mundime ino. Kunena kuti Nayenso anagwiritsa ntchito mau akuti "Chisautso chachikulu" kuchokera pa Mateyu 24:15-

26.Apa, akunena za nthawi ziwiri za chisautso chimene. Poyamba za nthawi ya kuuka kwa a Yuda pansi paulamuliro wa Maccabees, kuti ndicho chiyambi cha kuuka kwa chionongeko cha wotsutsa Kristu, pamene Kristu mwini akudza muulemerero wake. Kutanthauza kuti zidzachitika kuyambira nthawi ino, kufikira nthawi yamtsogolo yomwe siikudziwika.Apa ndipo pamene Ambuye wathu akubweransokudzaonongawotsutsa Kristu. Tikunena kuti Ambuye wathu Yesu Kristu akubwera ngati mutu wa mpingo wake komanso ngati mtetezi.

Ichi, ndichifukwa chake mngelo wa Mulungu akumuuza Danieli kuti bwezi la mpingo wa Kristu, mngelo Mikaeli amene wakhala akuonetsa kale ubwezi umenewu, m'mwamba, koma pano akuonetsa pansi pano pamene akuimirirakuthandizakuombola a Yuda pamene akuona kuti mphamvu yawo yachepa. Apa, ndipo pamene Mwana wa munthu adzaonetsedwaakuononga ntchito yonse ya m'dierekezi.

Wokondedwa anzanga apaulendo, Mwana wa munthu uyu, ndiye amene anadza ku anthu a mtundu wake, kudzakhala tchimo ndi temberero m'malo mwawo. Ndipo lero

m’mwambamoakuimabem’malo mwawo kuwapempherera kufikira chionongeko cha Antiokasi, amene akuonetsedwa kuti ndiye wotsutsa Kristu, ndipo adzaimabe m’nthawi yamtsogolo mpaka kudza kwake kachiwiri, pamene adzapulumutsa anthu ake onse, kwamuyaya.

Nkhani ikunena kuti pamene Kristu abwera kachiwiri, akudzabwezera chilango kwa onse amene akhala akunzuza anthu ake. Apa, ndipo pamene kudzakhala masautso osaneneka, amene asanaonekensom’mtundu wa Israeli wonse. Ichi, chidzayambika ndi kuonongeka kwa Yerusalemu, chomwe Ambuye Yesu akutchula pa Mateyu 24:21, pamene akuti, “Pakuti pomwepo padzakhala masauko akuru, monga sipadakhaleotero kuyambira chiyambi cha dziko, kufikira tsopano, inde ndipo sipadzakhalanso.” Iyi, ndiyo nkhani yomwe akunena Danieli 9:27, pamene akuti, “Ndipo iye adzapanganachipanganocholimba ndi ambiri sabata limodzi; ndi pakati pa sabata adzaleketsa nsembe yophera ndi nsembe yaufa; ndi paphiko la zonyansapadzafika wina wakupasula, kufikira chimariziro cholembedweratu, mkwiyo udzatsanulidwa pa wopasulayo.” Kunena kuti ichi, chidzachitika pamene Kristu

adzakhala atangokhazikitsa Ufumu wa Uthenga Wabwino padziko lapansi. Ichi, ndichilango chomwe chidzatentha ngati ng'anjo, kutha ndi kumwetula wodzikweza wokha ndi wonse wochita kusaweruzika. Kutsimikiza kuti apa, ndipo pamene Mikaeliadzaimira anthu a Kristu, nthawi yomwe sadzaimira anthu wotsutsaKristuyo.

Apa, ndipo pamene wokhulupirira ochepa a mtundu wa Israyeli, adzapulumutsidwa monga Ambuye adanena pa Mateyu 24:22, pamene anati, "Ndipo akadalekakufupikitsidwa masiku awo, sakadapulumuka munthu ali yense: koma chifukwa cha osankhidwawo masiku awo adzafupikitsidwa." Ndipo Yohane pa Chibvumbulutso 7:4, ndipo akutsindika kunena kuti, "Ndipo ndinamva chiwerengero cha iwo osindikizidwa chizindikiro, zikwi makumi khumi ndi makumi anayi mphambu anayi, osindikizidwa chizindikiro mwa mapfuko onse a ana a Israyeli."

2. Ndipo ambiri a iwoogona m'pfumbi lapansi adzauka, ena kumka ku moyo wosatha, ndi ena ku manyazi ndi mnyozowosatha.

Iyi, ndi nkhani ya kuuka kwa akufa,woyera mtima ndi wochimwa a m'Chipangano Chakale. Ichi, ndichimene akutanthauza pamene akuti, "Ndipo ambiri a iwo ogona m'pfumbi lapansi adzauka, ena kumka ku moyo wosatha, ndi ena ku manyazi ndi mnyozowosatha." Komanso idzakhala nthawi yomwe wokhulupirira a Israyeli wokhala m'nthawi ya chisautso chachikulu, adzapulumutsidwa pamodzi ndi khamulochuluka la anthu amitundu ina, amene adzakhala atapulumutsidwa nthawi imeneyo. Kutanthauza kuti a Yuda amene anafa a m'Chipangano Chakale, amene anakhulupirira pamodzi ndi anthu amitundu ina, amene anafa m'Chipangano Chakale, adzauka ndi kukhala ku moyo wosathapakumaliza pa chisautso chachikulu.

Tere, ndifuna kunena kuti woyera mtima a m'Chipangano Chakale sadzatengedwa panthawi ya mkwaturo ayi, popeza Paulo pa 1 Atesalonika 4:14, akunenetsa kuti, "Pakuti ngati tikhulupirira kuti Yesu adamwalira, nauka, koteronso Mulungu adzatenga pamodzi ndi Iye iwo akugona mwa Yesu." Ndipo pa verse 16, Paulo akutsindika kuti, "Pakuti Ambuye adzatsika Kumwamba mwini yekha ndi mpfuu ndi mau a mngelo wamkuru ndi lipenga la

Mulungu; ndipo akufa mwa Ambuye adzayamba kuuka.”Apa, ndipamene tikunena kuti kubwera kwa Ambuye kachiwiri, ndiko kumene kudzapulumutsa Israyeli yense wa Mulungu (Agalatiya 6:16).

Tikunena kuti wokhulupirira onse ali mwa Kristu mwa ubatizo wa Mzimu woyera umene unayambika pa tsiku la Pentecost umeneudzatha kapena udzafikira tsiku la mkwaturo. Ndiye tikuti gulu ili la anthu ndi lomwe likupanga mpingo wa Kristu. Tsono mwina inu muli kakasi ndi funso lakuti, chifukwa chiyani pamene mpingo udzakwatulidwa kuchoka m’dziko lapansi, pamene wokhulupirira a m’Chipangano Chakale adzakhala asanaukitsidwe? Yankho likuti popeza nthawi yakulowamuUfumuinaikidwa pakutha pa chisautso chachikuru, pamene Kristu akubwera kudzakhazikitsa Ufumu wake pansi pano. Apa, ndipo pamene Abraham, Isake ndi Yakobo adzaukitsidwa ndi kulowa muUfumu wa padziko lapansiwu.

3. Ndipo aphunzitsiadzawala ngati kunyezimirakwathambo; ndi iwo otembenuza ambiri atsate chilungamo ngati nyenyezi ku nthawi za nthawi.

Ndime iyi, ikuonetsa chithunzi chakuti atumiki a Mulungu pamodzi ndi woyera mtima, amene analandira chifundo kwa Iye, mwa chikhulupiriro, m'nthawi ya Chisautso Chachikulu, adzawala ngati kunyezimira kwa thambo. Umu, ndimo inu ndi ine, tiyenera kuchitira lero lino pamene tikukhala m'dziko lino. Monga Paulo pa Afilipi 2:15, akuti, "Kuti mukakhale osalakwa ndi oona, ana a Mulungu opanda chirema pakati pa m'badwo wokhotakhota ndi wopotoka, mwa iwo amene muonekera monga mauniko m'dziko lapansi." Kunena kuti wokhulupirira m'masiku amenewo adzakhala mboni za Yehova m'dziko lapansi, amene adzathandizira ambiri ku chilungamo cha Mulungu. Kutsindika kuti pamene akristu anyezimira m'dziko lino, anthu ambiri amatembenukirakwa Kristu, amene ali chilungamo cha Mulungu. Kutanthauza kuti chilungamo chanu ndi changa, "…ziri ngati chobvala chodetsedwa (Yesaya 64:6)." Kutsimikiza kuti ife tikhoza kudziona kulungama, koma chilungamo chathu ndi chodetsedwa m'maso a Mulungu.

Wokondedwa anzanga apaulendo, inu ndi ine, tikhoza kumalimbikitsana ndi kumanena kuti tikuchita chilungamo, koma tiyenera kudziwa kuti Mulungu sabvomereza ntchito zathu, koma

chilungamo cha Kristu chokha, chimene chingalandiridwemwachikhulupiriro. Kunena kuti pali ulemerero wa Mulungu, umene unasungidwira kwa woyera mtima wonse, amene ali anzeru ndi miyoyo yawo kwamuyaya.

4. Koma iwe Danieli, tsekera mau awa, nukhomere chizindikiro buku, mpaka nthawi ya chimariziro; ambiri adzathamanga cha uku ndi chauko, ndi chidziwitso chidzachuruka.

Pano pali nkhani yakutsekedwa kwa buku la ulosi kufikira nthawi yotsiriza. Iyi, sinthawiyakuthakwa nthawi yapansi pano ayi, koma nthawi yotsiriza yomwe buku la likuonetsa sabata la chisanu ndi chiwiri. Tere, ndizoona kuti pali zinthu zambiri zomwe inu ndi ine, sitikudziwa, koma zidzatsegulidwa pamene tidzafikapamzere wina. Ichi, ndichifukwa chake inu ndi ine, tiyenera kuika maso athu pa chinthu chimodzi chokha monga akunena Paulo pa Tito 2:13, pamene akuti, “Akulindira chiyembekezo chodala ndi maonekedwe a ulemerero wamkuru ndi Mpulumutsi wathu Yesu Kristu.”

Ndiye tikunena kuti zinthu za Mulungu zomwe zikuoneka kuti ndizosabveka bwino, patsogolo pano zidzaonetsedwa bwino ndi kukhala zomveka bwino.

5. Pamenepo ine, Danieli ndinapenya, ndipo taonani, anaimapo awiri ena, wina m'mphepete mwa mtsinje tsidya lino, ndi mnzake m'mphepete mwa mtsinje tsidya lija.
6. Ndipo wina anati kwa munthu wobvalabafuta,wokhala pamwamba pa madzi amumtsinje, chimariziro cha zodabwitsa izi chidzafika liti?
7. Ndipo ndinamvamunthuyowobvalabafuta wokhala pamwamba pamadzi a mumtsinje, nakweza dzanja lake lamanja ndi lamanzere Kumwamba, nalumbira pa Iye wokhala ndi moyo kosatha, kuti zidzachitika nthawi ndi nthawi zina ndi nusu; ndipo atathakumwaza mphamvu ya anthu opatulikawozidzatha izi zonse.

Ndime izi, zikutionetsa masomphenya aja Danieli adaona koyambirira kwa chapter 10. Mukumbukira tidanena kuti munthu wobvalazonyezimira ndi Kristu asanabvale thupi la munthu. Uyu, ndiye wina wa anthu awiriwa amene ali patsidya lina la mtsinje wa Tigris. Ndiye pamene mngelo winayuakufunsa kuti, padzakhala nthawi yotalika motani zinthu zonsezi zikuchitika? Tere, Kristu akuyankha kuti zidzachitika m'zaka zitatu ndi theka, yomwe ndi

nthawi ya kumapeto kwa zaka makumi asanu ndi awiri (70 years) a kumapeto kwa moyo wa Danieli. Apa, ndipo padzakhala kutha kwa kuukira kwa Israyeli kumene kudzaphwanyika pakutha pa nthawi ya chisautso chachikuru, pamene anthu ambiri adzabwera kwa Ambuye.

8. Ndinachimva ichi, koma osachizindikira; pamenepo ndinati Mbuye wanga, chitsiriziro cha izi nchiyani?
9. Ndipo anati, pita Danieli; pakuti mauwo atsekedwa, nakhomedwera chizindikiro mpaka nthawi ya chitsiriziro.

Tsono nkhani ikuti ngakhale Danieli ndiye anachitira umboni wa zinthu zonse zomwe zinaonekazo, koma sanathe kuzindikira chimene anamva ndi kuona. Tere Danieli sanamvetse kotero kuti anali kufunitsitsa kudziwa momwe zinthu zimenezi zidzachitikira. Koma Danieli akukumbutsidwa kuti zinthu zonsezi zidzachitika m'nthawi yotsiriza, kotero kuti pakali pano zakhomeredwa kapena kuti zatsekeredwakwa kanthawi pang'ono.

Nkhani yonseyi ikunena kuti Mulungu adzamulekererakayewotsutsa Kristu ndi cholinga chakuti achotse mphamvu ya anthu ake. Apa, ndipo pamene adzakwaniritsa mau

ake. Kutsimikiza kuti nthawi yabwino ya Mulungu yolanditsa ana ake, ndipamene masautso awo afika pachimake.

10. Ambiri adzadzitsutsa ndi kudziyeretsa, nadzayesedwa ndi moto; koma oipa adzachita moipa; ndipo palibe m'modzi wa oipa adzazindikira; koma aphunzitsi ndiwo adzazindikira.

Tikunena kuti pamene tiona momwe zinthu zikuyendera m'dziko lathu ndi momwe mpingo wa Mulungu ukuyendera, sitingalephere kufunsa kuti, kodi zinthu zimenezi zidzatha liti? Ambiri timaganiza kuti zinthu zimenezi, zidzathamoipira Ufumu wa Mulungu pakati pa ana ake, ayi ndithu sizidzatero. Kutsindika kuti choonadi ndi choonadi ndithu, kotero kuti chidzatumphuka ngakhale patapita nthawi yotalika motani.Kutsimikiza kuti ulamuliro ndi mphamvu zonse zogalukira Mulungu zidzaponderezedwa ndipo chiyero m'chikondi ndicho chidzaonekakunthawi za muyaya.

11. Ndipo kuyambira nthawi yotiidzachotsedwa nsembeyachikhalire, nichidzaimikachonyasachakupululutsa, adzakhalanso masiku chikwi chimodzi mphambu mazana awiri kudza makumi asanu ndi anayi.

Ndime ino ndiyofunika kwambiri chifukwa ndiyo Ambuye Yesu anali kunena pa Mateyu 24:15, pamene anati, “Chifukwa chake m’mene mukadzaonachonyasa cha kupululutsa, chimene chidanenedwa ndi Danieli mneneri, chitaima m’malo oyera iye amene awerenga m’kalata azindikira.” Kunena kuti kukhazikikakwachonyasam’kachisi, ndicho chizindikiro kwa wokhulupirira kuti chisautso chachikuru chayamba.

Taonani m’nthawi ya Danieli, panapita masiku 1,290 fano la chirombo lili chiimire m’Kachisi.Kotero kuti pakutha pa nthawi iyi, masiku awa kumapeto a chisautso chachikulu, ndipo pamene wotsutsa Kristu adzaponyedwam’nyanja ya moto.

13. Koma iwe, muka mpaka chimariziro; pakuti udzapumula, nudzaima m’gawo lako masiku otsiriza.

Danieli pano monga muja Ambuye Yesu adauza Simon Petro, kuti adzafa ndipo kuti sadzakhala ndi moyo kufikira Ambuye adzabweranso ndi kuukitsidwa ndi kulowa muulemerero.Momwemonso pano Danieli akuuzidwa kuti adzafa ndipo kuti adzaima mgawo lake m’masiku otsiriza.

Wokondedwa anzanga apaulendo, ndifuna titsirize ndi mau akuti, pamene Danieli akuuzidwa kuti adzaima m'gawo lake, akunena kuti iyeyu monga wokhulupirira wa m'Chipangano Chakale, adzauka pamodzi ndi woyera mtima a m'Chipangano Chakale pakuyamba kwa ulamuliro wa zaka chikwi pansi pano. Kutanthauza kuti sadzakwatulidwa pamodzi ndi mpingo wa Kristu, popeza chiyanjano chake ndi Mulungu, sichinadza mwa ubatizo wa Mzimu Woyera monga muja zinali patsiku la Pentecoste.

Koma pamene mau akunena za masiku otsiriza, akutanthauza kuti idzakhala nthawi momwe anthu ambiri adzalowamuUfumuwa Yesu Kristu. Anzanga, nthawi yamtsogolo yomwe ikunenedwa pano ndi ino, kotero kuti inu ndi ine tiyenera kudziwa kuti Ambuye akubwera ndithu kudzakhazikitsa Ufumu wake pansi pano umene udzakhala zaka chikwi.Ichi, chiyenera kukhala chiyembekezo chanu ndi changa.

Kwalerotilekeza pano. Ndipo tinali kusanthula Danieli 12:1-13, momwe timakambirana za chibvuto chachikulu ndi kutsekedwa kwa ulosi. Tere, lero tatsiriza bukuli lolembedwa ndi mneneri Danieli, momwe taona ulosi wokhudza masiku otsiriza.

Ambuye akuthandizeni inu kubvetsa ndi kuchita chifuniro chake.amen!